Diploma Programme
Programme du diplôme
Programa del Diploma

# Chichewa A: literature – Standard level – Paper 1
# Chichewa A : littérature – Niveau moyen – Épreuve 1
# Chichewa A: literatura – Nivel medio – Prueba 1

Wednesday 4 May 2016 (afternoon)
Mercredi 4 mai 2016 (après-midi)
Miércoles 4 de mayo de 2016 (tarde)

1 hour 30 minutes / 1 heure 30 minutes / 1 hora 30 minutos

---

**Instructions to candidates**

- Do not open this examination paper until instructed to do so.
- Write a guided literary analysis on one passage only. In your answer you must address both of the guiding questions provided.
- The maximum mark for this examination paper is **[20 marks]**.

**Instructions destinées aux candidats**

- N'ouvrez pas cette épreuve avant d'y être autorisé(e).
- Rédigez une analyse littéraire dirigée d'un seul des passages. Les deux questions d'orientation fournies doivent être traitées dans votre réponse.
- Le nombre maximum de points pour cette épreuve d'examen est de **[20 points]**.

**Instrucciones para los alumnos**

- No abra esta prueba hasta que se lo autoricen.
- Escriba un análisis literario guiado sobre un solo pasaje. Debe abordar las dos preguntas de orientación en su respuesta.
- La puntuación máxima para esta prueba de examen es **[20 puntos]**.



2216 – 0523
© International Baccalaureate Organization 2016

International Baccalaureate®
Baccalauréat International
Bachillerato Internacional

https://xtremepape.rs/

Lembani ndemanga pa nkhani **imodzi** yokha. Poyankha funsoli mugwiritse ntchito mafunso onse awiri amene aperekedwa.

**1.**

**Nyanga ya Nsatsi**

Mwachisangalalo koma ndi mitima yam'mwamba chifukwa chachitenthe posadziwa chomwe chingapse kumaulako, anyamata aja anayamba masewero a juga aja madzulo amenewo. Monga momwe ananenera Chagwa iye anasitikadi malaya ake. Sipanapite nthawi juga inatha, chovala chija chinapita. Anatenga ndi Felani. Chuma pa chuma chinzake. Ndithu, paja adati mvula ikakuona litsiro siikata.

Chagwa maganizo sanawapeze. Malaya anali omwewo omwe analanditsawo moti kopanda malayawo ndiye kuti iye adakamayenda mimba ili pamtunda. Izi sanafune kuti zitero ngakhale nthawiyi nkuti mimba ndi nthiti zomwe zili pamtunda. Iye anafuna njira yopezera Malaya akewo. Mutu wa Chagwa unkaganiza mofulumira kwambiri makamaka m'mavuto ngati amenewa. Chilichonse choti n'kusitika, kupatula bulangete ndi buluku panalibe.

Maganizo adamufikira Chagwa. Juga imayenera kupitirira mwanjira iliyonse. Zivute zitani. Popeza anzake enawo anali am'mphala okhaokha, Chagwa sadakayike kuti atasitika mkazi wake, Elube, palibe angadzakana. Yemwe angadzamuwineyo, mwanjira iliyonse mkaziyo angadzamutenge. Chagwa anafotokozera anzakewo kuti iye asitika mkazi wake wa kumudzi, yemwe angadzachite mwayi, adzamukwatira mkaziyo ndipo iye, Chagwa sadzanyinyirika.

Ndikhoza kulolera kuti usiku omwe uno tipite kumudzi kuti munthu wopambanayo akamuwone ndi kumutengeratu mkaziyo," anatero Chagwa.

Popeza anzakewo anali am'mphala okhaokha, panalibe zochedwa. Aliyense mwa anzakewo adaponya ndalama zawo zomwe anagwirizana. Juga idayambika. Chagwa nkuti akupemphera kuti zinthu zimuyendere bwino. Sanafune kutaya mkazi mwa njira ya juga. Uku nkutaya udzu bomwetamweta. Monga poyamba pomwe paja, juga siyinakhalitse. Idatha msanga, koma opambana anali wina. Zembere ndiye adapambana. Apa ndiye kuti Zembere ndi yemwe anachita mwayi wotenga Elube, mkazi wa Chagwa ngakhale mkaziyo anali asadamuwone.

Chagwa maganizo ake adazunguzika. Adawoneka wachisoni kenaka wokwiya chifukwa chopeza mkazi. Chagwa tsopano adazindikira kuti anachita zopusa positika mkazi. Sadakayenera kutero. Elube anali wapamtima wake ndipo sadakalolera kuti wina wake amutenge. Tsopano adamanga mfundo kuti zivute zitani Elube anali wake. Zembere samutenga.

"Koma samutenga mkazi wangayo," anatero mokwiya Chagwa akuwona Zembere akungodumphadumpha ndi chisangalalo nkhope itachita kuwala. Kwinaku amakhala ngati akumunyogodola Chagwa chifukwa cha kulanditsa mkazi.

"Ine nditenga mkaziyo," adayankha Zembere.

"Sutenga, ndiwako?"

"Eee ndiwanga mmayesa ndapambana ndine?" Zembere adatero mosangalala.

"Inde wopambana ndiwe koma mkazi wangayo ayi."

"Koma chinali chipangano."

"Chinalidi chipangano," anatsirira umboni Felani. "Chipangano chinayenera kulemekezedwa ndi kutsatidwa."

"Zoonadi," anatero Zembere.

"Chabwino kaneneni kulikonse kuti ndakukanizani mkazi," Chagwa adakalipa.

"Nkhani ya juga nkukayinena kuti?" Zembere adafunsa. "Kukakhala kupolisi sikukadzipereka tokha kumeneko?"

https://xtremepape.rs/

“Eee n’kukadziperekadi,” Felani anavomereza. “Koma ine ndikuti mkazi wanga simutenga, kaneneni kulikonse.”

Chagwa anawonekadi wokwiya. Iye anali wamtalipo ndiponso wadzitho koposa anzake aja. Mawonekedwenso ankakhala ngati mnyamata wolimba pa nkhani ya zigogodo. Chifukwa cha ichi anzake aja anachita mantha. Sanafune kukangana naye mopitiriza pozindikira kuti ndi momwe zinalilimo, Chagwa adakayibutsa ndewu. Nkhaniyi idangozizirira momwemu.

Elube tsopano anatopa nkudikira yankho lochokera kwa mwamuna wake. Iye anangosanduka nsanza zokhazokha ndipo kuyera kuja kunankira motumbuluka. Komabe anali msungwana wokongolabe. Amatha kumwetulira bwino, kumwetulira komwe kumawonetsa mano ake oyera ndi otsatana bwino. Kumwetuliraku nkomwe kumathandiza kuwalitsa nkhope yakeyo.

Tsopano Elube anali munthu womvetsa chisoni kwa pafupifupi munthu aliyense yemwe ankamudziwa bwino. Makamaka anthu omwe ankamuona ali pasukulu ndiponso asanakwatiwe ndiwo anankirankira kumumvera chisoni. Ndithu banja linamupundula mwana wa eni ake. Ena ankanyoza Chagwa potenga mkazi yemwe sanali womuyenera mmalo mosiyira anthu ena oti nkumutha kumusamala.

Chofuna banja chinamuthera Elube koma adapitirira kubisa maganizo akewo pozindikira kuti ofunika kudziwa zimenezo sanali makolo a Chagwawo koma Chagwa mwini wakeyo. Elube adakhulupirira kuti atalekedwa kaya kusudzulidwa akhoza kudzapeza wina mwamuna. Komabe maganizo amenewa amamuwawitsa mutu. Nkhani ya banja idamutinkha. Sanayifunenso. Adafuna kungolekeratu zabanja nkukayambanso sukulu kuti adzapite ku sekondale monga asungwana ena anali nawo ku sukulu aja. Elube ankalota zodzakhala mphunzitsi kapena nasi wa ku chipatala atadzamaliza maphunziro ake. Koma ankalemba m’madzi chabe. Malotowo sadakadzachitika. Izi zidakatero popeza panalibe sukulu yomwe imalemba ana asukulu othawa m’banja, kapena asungwana amene asudzulidwa kapenanso asungwana awana monga iyeyo. Akalingaliranso zimenezi amafunananso kulira pozindikira kuti chifukwa chothamangira kukwatiwa adadziyitanira mavuto ndiponso kudzitsekerezera zabwino zakutsogolo.

Whytone Kamthunzi, *Nyanga ya Nsatsi* (1990)

(a) Munganenepo chiyani pa momwe njira zosonyezera amtengambali (anthu amunkhani) zikuthandizira kupereka kapena kutambasula uthenga waukulu wa mu nkhaniyi?

(b) Fotokozani momwe mlembi wagwiritsira ntchit luso la kalembedwe monga kuyankhulana, pothandiza kusonyeza zomwe zikuchitika m’nkhaniyi.



https://xtremepape.rs/

**2.**

**Siananso Awa**

Si ananso awa
Siananso awa
Awona zoopsa
Amva zozizwitsa
Moyowu wawalawitsa zowawa
Chalochi chawakhudzitsa zopweteka
Siananso awa

Mavuto awakhwimitsa
Powatsekula m'maso
Zipsinjo zawatukula makutu
Matenda awathetssa msinkhu

Zokhoma zonse aziona
Zozunza zochuluka azikumana
Makolo osasamala awalilitsa
Akulu odzikonda awalilitsa
Siananso awa

Mawanga a dziko awaona
Owanamiza angotaya nthawi
Owaphimba m'maso angodzinyenga
Chosadziwa iwo simungachiloze

Benedicto Wokomaatani Malunga, *Siananso Awa* (2013)

(a) Perekani maganizo anu pa nkhani zazikuluzikulu zimene zili mu ndakatulomu komanso momwe kugwiritsa ntchito kuphiphiritsa kungathandizire kumvetsa bwino nkhanizi.

(b) Fotokozani njira zimene mlembi wagwiritsa ntchito pa kalembedwe ka ndakatuloyi komanso zotsatira zake.

https://xtremepape.rs/